

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO
KUPITA KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO

UNDIPATSE MTIMA WAKO


Dzuwa loswa mtengo linawala pa miyala ya m'mbali mwa phiri pamene Yesu ndi ophunzira ake amayenda mumseu wa dothi. Lidaali tsiku lalitali ndipo iwo anali otopa chifukwa cha khwimbi la anthu amene amabwera kwa iwo.

Mwadzidzidzi, munthu wolemera atavala za mtengo wapatali anafika kwa iwo akuthamanga. Ali wefuwefu kupuma, anadzagwada pansi pamapazi a Yesu. Moyembekezera zabwino, iye anafunsa kuti, “Mphunzitsi Wabwino, ndidzachita chiyani kuti ndilandire moyo wosatha?”

Yesu anaima ndipo anamuyang'ana ndi chisoni ndipo anati, “Udziwa malamulo...” Ndipo ndi mtima wonse mnyamatayo anati, “Usaphe, Usachite chigololo, Usabe, Usachite umboni wakunama, Usanyenge, Lemekeza atate wako ndi amako.”

Yesu anatembenukira kumbali akuganiza mozama, ndipo amalingalira za munthuyo. Iye amadziwa kuti munthuyo anali wolamulira ndipo anali ndi chuma chochuluka. Iye zinamukhudza kuti munthu uyu wabwino wachinyamata anadzichepetsa ndipo anali ndi mtima wofuna kukondweretsa Mulungu. Ndi mau achikondi, Yesu anati, “Usowa chinthu chimodzi: gulitsa ziri zonse uli nazo, nuga-wire osauka; ndipo udzakhala nacho chuma

cheni cheni m'Mwamba; ndipo ukadze kuno, unditsate Ine.”



*Khalidwe labwino komanso
kungotsatira ndondomeko
zabwino za malamulo
sizikwanira kuti munthu akalowe
ku moyo wosatha.*

Atamva izi, munthu waulamulirowo anakhumudwa ndipo nkhope yake inagwa pansi pamene amaimirira chifukwa cha kusautsika m'maganizo. Iye anavutika ndi chisoni chifukwa amafunitsitsa kutsatira Ambuye. Komabe, anali ndi chuma chochuluka ndipo sanali wokonzeka kuchigulitsa. Misozi ya chisoni idalengeza m'maso mwake, kenaka anapukusa mutu wake ndipo anachokapo nkumapita. Maso a Yesu

anadzala ndi chisoni pamene anamuona munthuyo akupita.

Ngakhale Yesu anayamikira khalidwe labwino ndi lokoma la munthuyo, anadziwa kuti izi sizingamupangitse kuti iye akalowe Kumwamba. Munthuyo amayenera kupereka mtima wake wonse ndi kukonda Mulungu koposa zina zilizonse pa moyo wake. Mulungu amafuna kuti achite ufumu pa zonse zimene mnyamatayo amazikonda. Yesu amadziwa kuti kupanda izi, penapake chikondi cha munthuyo pa zinthu zapadziko chidzasokoneza chikhumbokhumbo chake chofuna kutsata Ambuye. Nchifukwa chake Yesu anamuza za tanthauzo la kumutsata lye.

Khalidwe labwino komanso kungotsatira ndondomeko zabwino za malamulo sizikwanira kuti munthu akalowe ku moyo wosatha; ngakhale kungokhala ndi chikhumbokhumbo cha zinthu za Mulungu sikukwanira ayi. Zimatengera kudzikhuthula mwachikondi kuti munthu atsate Yesu ndi kukalowa Kumwamba. Tikhoza kukhala ndi mtima wolakalaka Mulungu, tikhozanso kukhala ndi chikondi cha muyeso wabwino, tikhoza kukhala abwino kwa amuna kapena akazi athu, nzika zabwino komanso ma neba

(Zapatirira pa tsamba 2)

Mau a Mkonzi

Tsamba 3

Kusanthula Baibulo:
Ubale wa Chikondi

Tsamba 4

Nkhani yotsatana nayo:
Chokhumba chachikulu
cha Mulungu

Tsamba 5

Mafunso ndi Mayankho:
Kodi zitanthauza chiyani
kutaya chikondi
choyamba
Tsamba 7

Kodi Mukudziwa?

Mau a pa Nyengo yake

Tsamba 8

zimene BAIBULO limaphunzitsa za...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;

Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chihero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;

Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;

Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;

1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chihero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;

1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;

Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

abwino, koma zimafunika zoposa izi.

Choyambayamba Mulungu amafuna kuti alamulire zinthu zimene ife timayikapo mti-ma. “Mwananga, undipitse mtima wako, maso ako akondwere ndi njira zanga.” (Miyambo 23:26). Kumeneku ndi kulira kuchokera mu mtima wa Mulungu kuwalilira anthu – “Undipitse mtima wako.” Pamene tiyika chikondi chathu pa Mulungu, timamukonda ndi mtima wathu wonse, moyo wonse, maganizo athu ndi mphamvu zathu zonse. Pamene Mulungu akulamulira mtima wathu, amachita ufumu pa zimene timakonda, nthawi yathu, chuma chathu, maloto athu ndiponso malingi-riro athu. Tiyenera kumupanga kuti akhale woyamba pa kena kalikonse pa moyo wathu.

Masiku ano anthu ambiri amabwera ndi kumadzafunsa za Kumwamba monga mmene anachitira mnyamata wolemera uja. Ena amangochoka osafuna kuti apereke chikondi chawo chonse kwa Mulungu. Ena amakhala anthu odalilika mu mpingo – pa kuyimba, kupemphera, kuphunzitsa komanso nthawi zina ngakhale kulalikira; ko-mabe osapereka kwa Mulungu ‘chinthu chimodzicho’ chimene chimakhalabe chotchinga pa chikondi chawo kwa Mulungu.

Kodi chikondi chanu chili kuti lero? Kodi nanunso mukusowabe chinthu chimodzi? Kodi mwamtaya Mulungu? Mumpatse mtima wanu. Chilichonse chimene mungachisiye kuti mutsate Yesu chidzabwezeretsedwa m’moyo uno ngakhalelenso umene ukudzawo.

-mws

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizidwa m’dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata uyu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zoonza za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawo amene ali muyeso wovomerezeka wa chikhulupiriro. Amaphunzitsa chipulumu-tso ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maomboledwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kumene kumatsatirapo. Ndipo kumatithandiza kuti titsogolere, tiwongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chihero choonekera pa gawo lililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wovomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & Rene Smith

KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa kalata umene timasindikiza miyezi itatu iliyonse molingana ndi chitsogozo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa email, pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa www.thegospeltruth.us. Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma email a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mkonzi.

KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choonadi imasindikizidwa mu maiko osiyanasiyana kuti igawidwe m’maikowo. Ntchito yo-sindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zaufulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

Mau a Mkonzi



"Ndimkonda, popeza Yehova amamva mau anga ndi kupemba kwanga. Popeza amanditcherera khutu lake, chifukwa chake ndidzaitanira lye masiku anga onse." (Masalmo 116:1-2).

Ndili mwana wamng'ono, ndinapereka mtima wanga kwa Mulungu ndipo ndina-dzikhuthula ndekha ku chisamaliro chake. Ndimakumbukira bwino lomwe kuti ndi-malira chifukwa chakuti Mzimu Woyera amanditsutsa pa moyo wanga.

Ndinapemphera ndi mai anga kuti Yesu alowe mu mtima mwanga pamene tinali kumbuyo kwa chipinda chimene timaphunzirira Sunday School. Sikuti ndinachita zinthu zoipa zoopsa, komabe ndinafunikira chisomo chomwecho mumtima mwanga ngati cha munthu womwa mankhwala osokoneza bongo kapena chiledzerere. Pamene ndimakula, ndi kukhwima m'maganizo ndimakha-la ndi zovuta pa kukula kwa moyo wauzimu komanso zina zolepheretsa pa njirayo – monga mmene amachitira ambiri amene amapulumsidwa ali achichepere. Sindinataye chikhumbokhumbo changa chofuna kutumikira Mulungu komabe ndili mnyamata kambirimbiri ndinapita pa guwa pamene ndinakapemphera. Lero ndiyamika Ambuye chifukwa cha kukhulupirika kwa Mzimu wake. Monga imanenera nyimbo ija kuti "Mzimu ananditsogolera mosaphonyetsa ku dziko limene lero ndikhalamo." Ndinali ndipo ndikadali ndi njala yokhala pamaso pa Mulungu tsiku ndi tsiku, chifukwa ndikatsata maganizo anga ndisochera.

Ndimawakonda Ambuye ndipo ndimatenga kupezeka kwake mmoyo wanga kukhala chinthu chofunikira kwambiri kuposa moyo umene. Ambuye wakhala wokhulupirika pokumva liwu langa ndi kuyanka pemphero langa. Wachiritsa thupi langa, kundibweza kuchokera ku dzenje la manda, nandipatsa banja labwino, nkundipatsanso chakudya cha tsiku ndi tsiku; koma koposa zonse anapulumsa moyo wanga kuchokera ku ukapolo ndi nsinga za uchimo. Iye anandipatsa mtendere Wake ndi kupezeka kwa Mzimu wake. Zoonadi, ndili ndi zambiri zoti ndimuyamike nazo. Sizitengera kuti wakumana ndi mayesero kapena zokhumudwitsa zotani, ngati umakonda Ambuye, uli ndi chuma chamtengo wapatali kuposa zina zonse pa dziko lonse lapansi. Kalata uyu wa Gospel Truth akuyang'ana kwambiri za lamulo lofunikira kwambiri kuposa onse komanso chiphunzitsa chofunikira m'baibulo – Chikondi.

Pamene mukuyamba chaka chatsopanochi, mutsimikize kuti Mulungu adzakhala wokhulupirika kwa inuyo. Monga mmene wakumana ndi zosowa zanu mmbuyomu, nakutsogolerani pamene mumadutsa mzigwa ndi mmoto, momwemonso akhala nanu m'chaka chino. Mukhale okhulupirika, wotsatira wa Yesu, ndipo maso anu akhale chindunji pa Mbuye wanu. Zipambano zatsopano zikudikira inu ngati mumamatira pa Yesu, ndipo tsiku lina mudzayenda naye pa ulendo wokolowa Kumwamba.

Mu miyezi iwiri yapitayi, ndakhala ndikusautsika m'thupi langa ndipo sindinathe kutakataka chifukwa cha mutu wa mpwesa, kukomoka, ndi kufooka kwa thupi. Ndikuyamika Ambuye chifukwa cha kukhudza kwake pa ine ndipo yang'anani kutsogolo kumene kukubwera zambiri. Ndikulimbikitsika mwa Ambuye ndipo ndikukhumba kukhala ndi zaka zochuluka kuti ndigwire ntchito mu utumiki wake ngati lye andiyesa ine kukhala woyenera kuti andidalitse ndi moyo komanso mphamvu. Pemphero langa ndi lakuti Gospel Truth ikhala chilimbikitso ndipo ithandiza owerenga aliyense wokhala kuno komanso kutali. Ngati mwadalitsika ndi kalatayu, zingakhale zolimbikitsa mtsogolo muno kuti ndimve kuchokera kwa inu. Chonde masukani ndipo mukhoza kundilemba pa email iyi: Michael.w.smith@sbcglobal.net. Ambuye akudalitseni ndi chaka chopambana chifukwa cha kupezeka kwake. Tiyeni tiyende m'kuwala kwake ndi m'chiyero cha Mau ake ndipo tikhale pa mtendere.

Michael W. Smith
January 2013

Zambiri Zili pa
INTANETI

*Mukafuna kutipeza
pa intaneti, mulembe
www.thegospeltruth.us
kuti mudzilandira makalata
athu kapenanso kuti
muone makalata akale.*



MMENE MUNGAYATSIRE CHIKONDI CHANU PA MULUNGU

LAPANI

Muvomereze kuti mwayitirira ndipo mwataya chidwi chanu pa Mulungu. Lapani ndipo mupemphe Mulungu kuti akukhulukireni ndi kukubwezeretsani.
Salmo 51:12

FUNANI MULUNGU

Mubwerere ku moyo wokonda kuwerenga Malemo. Mupemphe Mulungu kuti abwezeretse mwainu njala ya choonadi ndi chilungamo.

KUMVERA

Mudule zinthu zonse zimene zinga kusuntheni kutali ndi Mulungu komanso kusokoneza cholinga cha moyo wanu. Kumvera ndi chisankho chimene mumapanga kuti mukonde Mulungu koposa zina zonse.

MUSALEKE KUYANJANA NDI ANZANU

Musaleke kupita ku tchalichi. Konzekeretsani mtima wanu ndi kusiya zisamaliri zonse za moyo uno pamene mupita ku nyumba ya Mulungu.

TUMIKIRANI ENA

Musalole kuti kudzikonda kukupangitseni kukhala aulesi muuzimu. Mupemphe Ambuye kuti akuthandizeni mmene mungawatumikire iwo amene mumakhala nao pafupi.

MUKHALE NDI CHIMWEMWE CHA CHIPULUMUTSO

Mukhale ndi mtima wa chiyamiko chifukwa cha madalitso a Mulungu. Tsiku lililonse muonetse chikondi chanu pa Mulungu mu zonse zimene mumachita.

KALOZERA POSANTHULA MAU A MULUNGU

MUTU – UBALE WA CHIKONDI

Mau a Mulungu: 1 Yohane 4:16-17 *Ndipo ife tazindikira, ndipo takhulupirira chikondicho Mulungu ali nacho pa ife. Mulungu ndiye chikondi, ndipo iye amene akhala m'chikondi akhala mwa Mulungu, ndipo Mulungu akhala mwa iye. M'menemo chikondi chathu chikhala changwiro kuti tikhale nako kulimbika mtima m'tsiku la mlandu; chifukwa monga lyeyu ali, momwemo tili ife m'dziko lino lapansi.*

Tanthauzo la Chikondi: Kukondana, kukoma mtima, ubwino, kulumikizana. Chisankho

1. Maganizo a Mulungu pa munthu

A. Yeremiya 31:3 Chimachokera ku chikondi chophatikiza ndi kukoma mtima.

B. Yeremiya 29:11-13 Maganizo a mtendere.

2. Chimene Mulungu amafuna pa Ubale

A. Genesis 3:5-8 Mulungu amafunitsitsa kuti tidziyanjana naye.

B. Chivumbulutsa 3:20 Onani, ndaima pa khomo.

C. 2 Akorinto 5:17-18 Kuyanjanitsidwanso ndi Mulungu.

3. Amene amakondedwa ndi Mulungu

A. Yohane 3:16 Dziko Lapansi.

B. Aroma 5:8 Ochimwa.

C. Aefeso 5:25 Mpingo.

4. Chionetsero cha chikondi cha Mulungu

A. 1 Yohane 4:9-10 Mulungu anatumiza Mwana wake mmodzi yekha.

B. 1 Yohane 3:1,16 Onani kukula kwa chikondi cha Mulungu.

5. Chikondi ndicho Lamulo lalikulu kuposa onse

A. Deuteronomo 10:12 Chikondi nchofunikira.

B. Mateyu 22:36-38 Muyenera kukonda Ambuye.

C. 1 Akorinto 13:1-3 Popanda chikondi.

6. Chikondi ndi Mphatso yochokera Kumwamba

A. 1 Yohane 4:7-8 Chikondi ndi chochokera kwa Mulungu.

B. Aroma 5:5 Chikondi chimaperekedwa ndi Mzimu Woyera.

7. Chikondi chili mu zintchito

A. 1 Yohane 3:18 Tiyeni tikondane m'ntchito ndi m'choonadi.

B. Mateyu 15:8 Ena amalemekeza ndi milomo yao chabe.

8. Mmene timaonetsera chikondi chathu

A. Yohane 14:15, 23-24 Adzasunga mau anga.

B. 1 Yohane 5:3 Ife timasunga malamulo ake.

C. 1 Yohane 4:20-21 Ife timakonda abale.

9. Sikungatheke kukonda Mulungu ndi Dziko

A. Mateyu 14:15, 23-24 Sitingathe kutumikira Ambuye awiri.

B. 1 Yohane 2:15-17 Osakonda dziko lapansi.

C. Deuteronomo 13:3 Ambuye atsimikiza za chikondi chathu.

10. Zizindikiro za Chikondi Chenicheni

A. 2 Akorinto 6:6 Chosanyenga.

B. 2 Akorinto 8:8 Choona.

C. 1 Timoteo 1:5 Chochokera mu mtima wangwiro.

11. Kukwaniritsidwa kwa Chikondi

A. Aefeso 3:17-19 Chidzalo cha Mulungu.

B. Yohane 15:10-11 Kuti chimwemwe chanu chikhale chochuluka.

12. Mphamvu ya Chikondi

A. 1 Yohane 4:18 Chikondi chenicheni chimathamangitsa mantha.

B. 2 Akorinto 5:14-15 Kukakamizidwa ndi Chikondi.

13. Ndi Chiyani chimalekanitsa Munthu ndi Chikondi cha Mulungu?

A. Aroma 8:35 Ndi chiyani chingatilekanitse?

B. Yohane 14:23-24 Kusamvera.

14. Kuchepa kwa Chikondi

A. Mateyu 24:12 Chikondi chidzazilala.

B. Chivumbulutsa 2:4 Mwataya chikondi chanu cha poyamba.

C. Chivumbulutsa 3:15-17 Muli ofunda.

15. Mphototho kwa iwo okonda Mulungu

A. Yakobo 2:5 Adzalandira cholowa cha ufumuwo.

B. 2 Timoteo 4:7-8 Korona wa chilungamo.

CHOKHUMBA CHA MULUNGU

(Tsatanetsatane wa mau othandizira pa kusanthula kwa Mau Mulungu)

MULUNGU AFUNAFUNA ANTHU

Kuchokera pachiyambi cha chilengedwe, Mulungu anafuna kuti akhale pa ubale ndi mtundu wa anthu. Timawerenga zakuti Mulungu amayenda mmunda wa Edeni mnthawi yamadzulo kufunafuna kuti ayanjane ndi kukhalira limodzi Adamu ndi Hava (Genesis 3:8-9). Ngakhale Babibulo lili buku la mbiri komanso lophunzitsa zamulungu, ilo ndi chifuniro cha Mulungu ndiponso kufunafuna chikondi ndi munthu.

UCHIMO UMAONONGA UBALU WA MUNTHU NDI MULUNGU

Mulungu analenga mtundu wa anthu ndipo chokhumba chake chachikulu chinali chakuti adzilumikizana ndi chilengedwe chake – osati mokakamiza kapena mouniriza, koma mwachikondi. Adamu ndi Hava sanamvere Mulungu ndipo uchimo wao unawalekanitsa iwo ku chiyanjano chabwino chimene anali nacho ndi Mulungu. Nthawi zonse uchimo umasokoneza ubale wa pakati pa Mulungu ndi munthu. Komabe, Mulungu sanafune kungotisiya choncho tili olekanitsidwa naye chifukwa cha uchimo ndi chisalungamo, zimene chilango chake ndi imfa.



MULUNGU ANATUMIZA MWANA WAKE KUDZATIYANJANITSANSO

Mulungu anatikonda kwambiri kotero kuti anatumiza Mwana wake mmodzi yekha ku dziko lapansi kuti adzatifere kuti ife tipulumuke (Yohane 3:16). Iye anafulumizidwa ndi chikondi ndipo chikondi cha Mulungu chilipobe mpaka lero lino. “Yehova anaonekera kwa ine kale, ndi kuti, Inde, ndakukonda iwe ndi chikondi chosatha; chifukwa chake ndakukoka iwe ndi kukukomera mtima” (Yeremiya 31:3).

ZOCHITA ZA MULUNGU ZIMATSOGOZEDWA NDI CHIKONDI

“Mulungu ndiye Chikondi” (1 Yohane 4:8) ndipo amachita momwemo pamene akhala pati pathu. Ena angathe kumuona Mulungu ngati bwana wankhanza – ongolamulira zinthu komanso ovuta kumukondweretsa. Chithunzi cha Mulungu chotere chimachokera kwa Satana. Mulungu ali Mulungu wa chikondi amene amasamalira chilichonse chimene chimakhudza miyoyo yathu. Iye amafika mwa chikondi kwa munthu wina aliyense posatengera mmene munthuyo aliri. Iye ndife osayenera chikondi chachikulu cha Mulungu ndipo palibe chimene tinachita kuti

tilandire chikondicho. “Koma Mulungu atsimikiza kwa ife chikondi chake cha mwini yekha m'menemo, kuti pokhala ife chikhaliwe ochimwa, Khristu adatifera ife” (Aroma 5:8).

CHIKONDI CHIMENE CHABWEZEDWA NDI CHOKWANIRA

Chikondi chimakhala chosakwanira ngati sichibwezedwa. Mulungu amatikonda koma ubale umenewo ndi osakwanira mpaka titamukonda Iye ndi mtima wathu wonse popanda china chilichonse choletsa. Katswiri wa malamulo uja anafunsa Yesu kuti, “Mphunzitsi, lamulo lalikulu ndi liti la m'chilamulo?” Ndipo Yesu anati kwa iye, “Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse. Ili ndilo lamulo lalikulu ndi loyamba” (Mateyu 22:36-38). Ziphunzitsa zina

zonse ndi zabodza pokhapokha ngati zakhazikika pa lamulo ili limene liri loyamba ndi lalikulu kwambiri. Anthu ambiri amatumikira Mulungu chifukwa choopa kapena pofuna kudzipereka ku mpingo wao kapena chikhulupiro chawo. Mu ubale wa chikondi, tipeza moyo wozama ndiponso waphindu. Tipezamo chikondi chimene chimatipangitsa

kuti tikhutire chifukwa ubalewo ndi wokwanira. Amenewa ndiwo magwero a mtendere weniweni ndi chimwemwe potumikira Mulungu.

CHIKONDI CHENICHENI SICHIKAKAMIZIDWA

Kalekale panali munthu wina amene amamumangirira mkazi wake ndi maunyolo ndi kumusiya ku khitchini tsiku lililonse iye akamapita ku ntchito. Iye amaona kuti mwina mkaziyo amuthawa ndipo kuti sabweranso. Ubale wao unali wa mantha ndi wa ukapolo. Zikanakhala bwino mwamunayo popita kuntchito akadamusiya mkazi wake namadziwa kuti adzamupezanso pobwera chifukwa chakuti mkaziyo amamukonda. Chimenechi ndicho chibale chimene Mulungu akufuna—ubale umene wina sakakamizidwa kukhala m'moyo wachiyero koma pamene munthu akhala mmoyo wachiyero chifukwa ali ndi mtima wa chikondi. Mphamvu ya chikondi ndi imene imakakamiza ana a Mulungu enieni kukhala moyo wachiyero (2 Akor. 5:14).

CHIKONDI CHATHU CHIMAONETSEDWA PA KUMVERA

Anthu ambiri amasendera kwa Mulungu ndi pakamwa pao ndi kumulemekeza ndi mlomo wao okha basi, koma pamene mitima
(Zapitirira pa tsamba 6)

(Kuchokera pa tsamba 5)

yao ili kutali ndi Iye (Mateyu 15:8). Chikondi chenicheni sichionetsedwa m'mau amene timalankhula koma kudzera mu zimene timachita m'moyo wathu.

Yesu anati, “Ngati wina akonda Ine, adzasunga mau anga” (Yohane 14:23). Chimenechi ndi chionetsero chenicheni cha chikondi mu dziko limene ambiri amanena kuti ndi ake a Khristu koma ochepa chabe ndi amene amamvera Mau a Mulungu. Pamene kumvera kwachepa, pameneponso ndiye kuti chikondi chachepa. Palibe chimene chingatilekanitse ndi chikondi cha Mulungu (Aroma 8:35) kupatula kusamvera kwathu (Yohane 14:23-24).

PALI MALO AMODZI OKHA PA “CHIKONDI CHOYAMBA”

“Palibe munthu angathe kukhala kapolo wa ambuye awiri” (Mateyu 6:24). Palibe malo mu ubale ndi Mulungu umene munthu amatsata za dziko kwinaku ndikumatsata Mulungu. Ngati munthu akonda zadziko, mwa iye mulibe chikondi cha Atate (1 Yohane 2:15-17).



CHIKONDI CHODZIKHUTHULA

Pamene anthu awiri akondanadi, amalolera kutaya nthawi ndi mphamvu zao kuti akhalire pamodzi. Chokhumba chao chimakhala kuti asangalatsane. Izi ndi mmene zimayenera kukhalira pa ubale wathu ndi Mulungu. Chikondi chimayenera kubweretsa mtima wopembedza ndi kutumikira Mulungu mwakufuna kwathu. Kumvera sikukhalanso chinthu chochitika pofuna kukwaniritsa ntchito, koma ndi chitsimikizo cha chikondi chathu. Chikondi chimabweretsa kukondwa, kukhutitsidwa ndi mphamvu pamene tikutumikira Ambuye.

IYE AMENE AMAKONDA MULUNGU AMAKONDANSO MBALE WAKE

Pamene anthu achizindira chikondi cha Mulungu, chikondi chake cha Mulunguyo chimawala mumtima mwawo monse kudzera mwa Mzimu Woyera (Aroma 5:5). Ubale umenewo umaonetsedwa osati pomvera Mulungu kokha, komanso pamene tikonda abale ena. Popeza ngati munthu sakonda mbale wake, chikondi cha Mulungu sichipezeka mwa iye (1 Yohane 4:20-21).

CHIKONDI CHANGWIRO CHIMATITSIMIKIZIRA ZA MOYO WOSATHA

Ubale wa chikondi ndi Mulungu sungobweretsa mtendere ndi chimwemwe mmoyo uno wokha ayi, umatitsimikiziranso za moyo wosatha. “Chotsalira wandiikira ine korona wa chilungamo, amene Ambuye, woweruza wolungama, adzandipatsa ine tsiku lijalo: ndipo si kwa ine ndekha, komatunso kwa onse amene anakonda maonekedwe ake” (2 Timoteo 4:8).

CHOKHUMBA CHACHIKULU CHA MULUNGU NDICHO KUKHALA PA UBALE NDI INUYO

Chokhumba chachikulu cha Mulungu ndi chakuti inuyo mukhale pa ubale weniweni ndi kukhala mnzake. Mulungu akufuna kukhala gawo lofunikira kwambiri pa moyo wanu. Chokhumba chake ndi chakuti inuyo mukhale ndi nthawi yomakhala naye ndi kucheza naye. Pali chiyanjano cha mtengo wapatali pamene mukhala pa ubale woterewu. Ubale ndi Mulungu, umene maziko ake ndi chikondi, udzapereka tanthauzo ndi cholinga chenicheni ku moyo wanu.

-mws

*“Popeza Yehova Mulungu wanu
akuyesani, kuti adziwe ngati mukonda
Yehova Mulungu wanu ndi mtima wanu
wonse, ndi moyo wanu wonse.*

*Muziyenda kutsata Yehova Mulungu
wanu, ndi kumuopa, ndi kusunga
malamulo ake, ndi kumvera mau ake, ndi
kumtumikira Iye, ndi kummamatira.”*

Deuteronomo 13:3-4

Mafunso ndi Mayankho

Funso: Kodi zitanthauza chiyani kutaya chikondi cha poyamba?

Yankho: Funso limeneli likupezeka mu Mau a Mulungu pa Chivumbulutso 2:4 pamene akuti: “Koma ndili nako kanthu kotsutsana ndi iwe, kuti unataya chikondi chako choyamba.” Mzimu wa Mulungu amalankhula ndi mpingo wa ku Efeso.

Muone ndithu kuti mpingowu unali utasutsana ndi choipa ndipo umachita zinthu zabwino zambiri ndiponso zolondola. Ngakhale unali omvera pa chikhulupiriro ndi mu chiphunzitso, Aefeso adataya chikondi ndiponso kuyanana kwao ndi Mulungu kumene adakhala nako kanthawi kena. Mabuku olongosera a JFB akuti “Kufunda kwa chikondi chao kunapangitsa kuti akhale ndi chiphunzitso chabwino koma chopanda moyo.”

Malemba nthawi zambiri amafanizira ubale wa pakati pa mwamuna ndi mkazi ndi ubale wa pakati pa Khristu ndi Mpingo. Tangoganizani chikondi chimene chimakhala pa banja la anthu amene angokwatirana kumene ndipo zimene amachita zimaonetsa kudzipereka kwawo. Iwo amafuna kungokhala limodzi ndi kudzipereka kwathunthu kwa wina ndi mnzake. Banja lawo limakhala lachimwemwe ndi lowala.

Ndi mmene zimakhala m’dziko lathu lauchimoli, mabanja ambiri amataya chikondi chawo ndi kukhulupirika kwawo. Amayamba kungokhalira limodzi mnyumba koma chikondi chinatha kalekale. Chimodzimodzi, izi zachitika kwa anthu

ambiri pa ubale wao ndi Mulungu. Munthu wina wakuti wangopulumutsidwa kumene amakhala ndi nthawi yopambana mmoyo wopanda koutsutsa wodzadza ndi mtendere komanso chisomo. Koma nthawi ikamapita, ngati ubalewo sukonzedwa, munthuyo akhoza kubwereranso ku moyo wake wauchimo kapena kumangochita ‘zinthu zabwino’ koma palibe chikondi ndi changu cha poyamba chija.

Iwo amene ataya chikondi chao cha poyamba akulamulidwa kuti alape. Pali mipingo ndi anthu ambiri amene aima njii

“Ambiri ataya chikondi chawo cha poyamba...”



Nthawi yao, mphamvu zao, zimene amalabadira ndi kukonda zakhazikika pa zinthu zina...

Mulungu wasanduka ‘chokondedwa chachiwiri’ – kapena osamukondanso.”

potsutsana ndi choipa, koma ataya moto wa chikondi umene unkayaka poyamba. Iwo ataya chenicheni chimene Mulungu amafuna kuti iwo achite – ubale wa chikondi.

Kumukonda Mulungu ndi mtima wonse ndi kumene kumabwezeretsa moto mu utumiki wathu wa kwa Mulungu. Tiyeni tisakodwe mu msampha wa kungokhala

ndi chiphunzitso cholondola komatu chopanda chikondi chake kuti chikhale chamoyo. Ubale umatenga nthawi. Uyenera kutetezedwa ku zinthu zimene zingalowe ndi kuwunonga.

“Ndipo chifukwa cha kuchuluka kwa kusaweruzika, chikondano cha anthu aunyingi chidzazirala” (Mateyu 24:12). Anthu ambiri ataya chikondi chao cha poyamba chifukwa iwo apereka chikondi chao ku zinthu za dziko lapansi pamene kwinaku akungosunga chiphunzitso choona. Mulungu amasanduka chikondi chao chachiwiri kapena osamukondanso. Nthawi yao, mphamvu zao, ndi chidwi chao komanso zonse zao zimakhazikika pa zinthu zina.

Izi zimabwezetsa moyo waulesi ndi wozilala potumikira Mulungu ndipo changu polalikira uthenga wabwino sichikhalapo. Amakhala ndi maonekedwe a chipembedzo. Ndi kofunikira kwambiri kudzipereka miyoyo yathu kuti tione ngati tikanali ndi chidwi pa za Mulungu ndi kuti sitinataye chikondi chathu cha poyamba.

Monga mmene mwamuna ndi mkazi amafunika kuti adzilankhulana ndi kukhala pamodzi kuti chikondi chao chikhale champhamvu, ndi chimodzimodzinso ndi Mulungu. Ndi kofunikira kuti titengulire chikondi chathu cha poyamba powerenga Mau a Mulungu, kupemphera, kulumikizana ndi Mulungu, ndi kumuika Mulungu patsogolo pa chisankho chilichonse chimene tingapange. Chopambana zonse, tiyeni tilole chikondi chikhale chimene chimatifulumizitsa pa utumiki ndi pa zabwino zimene timachita.


Ndi pokhapo pamene timvetsa za chikondi cha poyamba pamene tidzakhalira ndi changu powauza ena za uthenga wabwino ndi kudzoza kumene kumakhala kwa tsiku ndi tsiku. Izi zimapangitsa kuti chiphunzitso chikhale chamoyo komanso zimapereka chifukwa ndi chimwemwe chokhalira ndi moyo.

-mws



KODI MUKUDZIWA?

- ◆ **YEHOVA (YAHWEH pa Chihebri)** ndi dzina la umwini ndi lodziitanira la Mulungu mu Malemba.
– Mulungu waoyo, wokhala chikhalire, wosasintha, wamuyaya, mlengi ndiponso mwini wa zonse.
- ◆ **YESU** atanthauza ‘Mpulumutsi.’
- ◆ **EMANUELE** atanthauza ‘Mulungu nafe.’
- ◆ **MESIYA** ndi mau ochokera ku Chihebri amene atanthauza ‘wodzozedwa.’
- ◆ **KHRISTU** ndi mau ochokera ku Chigriki amene atanthauza ‘wodzozedwa.’ Ndi ofanana ndi Mesiya.
- ◆ **ALEFA NDI OMEGA** awa ndi lemba loyamba ndi lotsiriza pa kalembedwe ka chinenero cha Chigriki: Mauwa ndi amene amaimira Yesu monga chiyambi ndi chitsiriziro cha zinthu zonse.



Mau a pa

Nyengo Yake

Osati mwa Kuposa kwa Mau


KUTI MUTIPEZE

The Gospel Truth
605 Bishops Ct.
Nixa, MO 65714
USA
Email:
editor@thegospeltruth.us

CHIYERO KWA AMBUYE

1 Akorinto 2:1-5 Ndipo ine, abale, m'mene ndinadza kwa inu, sindinadza ndi kuposa kwa mau, kapena kwa nzeru, polalikira kwa inu chinsinsi cha Mulungu. (2) Pakuti ndinatsimikiza mtima kuti ndisadziwe kanthu mwa inu, koma Yesu Kristu, ndi lye wopachikidwa. (3) Ndipo ine ndinakhala nanu mofooka ndi m'mantha, ndi monthunthumira mwambiri. (4) Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m'chionetso cha Mzimu ndi cha mphamvu; (5) kuti chikhulupiro chanu chisakhale m'nzeru ya anthu, koma mu mphamvu ya Mulungu.

Charles Haddon Spurgeon, amene amadziwika kuti ndi “kalonga wa alaliki,” tsiku lina lamulungu anaganiza kuti sanalalikire bwino ndipo amadzimvera chisoni. Pamene amayenda kuchoka ku tchalitchi lake, chimene chinali chachikulu mu mzinda wa London, amadzifunsa ngati mu ulalikiwo mungapezeke chabwino chilichonse. Atafika kunyumba, anagwada pansi napemphera nati, “O! Ambuye Mulungu, Inuyo mungathe kupanga kenakake kuchokera ku chopanda kanthu. Chonde dalitsani uthengawo.”



Mu miyezi yotsatira, anthu 41 ananena kuti apanga chisankho chovomereza Khristu ngati Mpulumutsi chifukwa cha ulaliki uja “wosakhala bwino.” Lamulungu lotsitalo, pofuna kukonza “cholakwikacho,” Spurgeon anakonza ulaliki “wamphamvu” – koma zachisoni kuti palibe anadzipereka.

Zimene anakumana nazo Spurgeon zikutsendera mfundo ziwiri zofunikira kwambiri kwa iwo onse amene amatumikira Ambuye. Choyamba, tiyenera kukhala ndi mdalitso wa Mulungu pa zimene timachita. Solomo ananena pa Salmo 127:1, “Akapanda kumanga nyumba Yehova, akuimanga agwiritsa ntchito chabe.” Kachiwiri, kufooka kwathu ndiye nyengo zimene Mulungu amagwira ntchito mwa ife. Mtumwi Paulo anati, “Chifukwa chache ndisangalala m'maufoko, m'ziwawa, m'zikakamizo, m'mazunzo, m'zipsinjiko, chifukwa cha Kristu; pakuti pamene ndifooka, pamenepo ndiri wamphamvu.” (2 Akorinto 12:10)

Chakudya cha Lero, May 18, 1992